ttb_Nya_0889_script

Ezekiel : 7:1-8:4

Mutu : Ulosi wa chionongeko chotsiriza cha Yerusalemu

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau apa Amosi 8:15, amene akuti, “Ndipo ndidzawaoka m’dziko mwawo ndipo sadzazulidwanso m’dziko lawo limene ndawapatsa, ati Yehova Mulungu wako.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula Ezekieli 5:17-7:2, m’mene timaona za kuonongeka kwa mzinda wa Yerusalemu. Ndipo lero pa Ezekieli 7:1-8:4, tikambirana za ulosi wa chionongeko chotsiriza cha mzinda wa Yerusalemu.

Ezekieli 7

Ichi, ndi chapter momwe muli Uthenga wachiwiriwa chilango pa Israeli yense. Ngakhale Uthenga wa m’chapter 5, unali kukhudza Yerusalemu, koma pano Uthenga uwu, ndiwadziko lonse la Israeli. Ndiye tikunena kuti chilango cha m’mbuyomo sichidanthandize kuti anthu adze kwa Mulungu ayi.

1. Ndipo mau a Yehova anandidzera, akuti,

2. Ndipo iwe wobadwa ndi munthu, atero Ambuye Yehova kwa dziko la Israeli, kwatha; kwafikakutha kwake pa ngondya zinayi za dziko.

Pano Ezekieli akupereka Uthenga wachilango kwa Israeli yense, kuti chilango chikudza ndithu padziko lonse la Israeli. Kuphatikiza mapfuko khumi a kumpoto pamodzi ndi mapfuko awiri akum'mwera.Ndiye muulosi uwi, Ezekieli akunenetsa kuti ichi, ndicho chilango chotsiriza mu Yerusalemu ndi dziko lonse la Israeli.Kutanthauza kuti tsopano Yerusalemu adzaonongekakotheratu ndipo kuti anthu onse adzatengedwa ukapolo ku Babulo. Kutsimikiza kuti Mulungu akudza ndi masautso ochuluka pa mtundu wa Israeli.

3. Tsopano kwakudzerakuthakwako, ndipo ndidzakutumizira mkwiyo wanga ndi kukuweruza monga mwa njira zako ndipo ndidzakubwezerazonyasa zako zonse.

Pano ndifuna tigwire mau akuti, "ndidzakutumizira mkwiyo wanga ndi kukuweruza monga mwa njira zako."Ndiye ndifuna ndikufunseni kuti, kodi ndikothandiza motani kukhala mkristu ndi kumachita chinyengo? Kapena ndifunse kuti, kodi

palichokuthandizani inu, kukhala munthu wopembedza koma wosapulumuka? Yankho monsemu likuti palibe chothandiza, kotero kuti ndibwino kukhala m'nkhalango kumene munthu sadziwa china chilichonse cha Mulungu woona, koma milungu yosema basi.Ndiye chimene ndifuna kunena ndi chakuti, udindo wa mkristu ndi waukulu, popeza ndiye munthu amene adamva mau a Mulungu, koma amachita kukana mwadala. Ndiye muyenera kudziwa kuti pamene mkristu akumva mau a Mulungu kawiri-kawiri, ndipo pamene amalandira udindo waukulu.Kutsimikiza kuti munthu adzalandira chilango malinga ndi momwe akuchitira ndi mau a Mulungu. Mwanjira ina tikunena kuti munthu adzazindikira kuti akulandira chilango chifukwa cha zochimwa zake.

4. Ndipo diso langa silidzakulekerera, sindidzachita chifundo, koma ndidzakubwezera njira zako ndi zonyansa zako zidzakhala pakati pako; ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.
5. Atero Yehova Mulungu, choipa, choipa cha pa chokha, taona chirimkudza.

6. Kuthakwafika, kwafikakutha.
7. Tsoka lako lakufikira, nzika iwe, yafika nthawi, tsiku liri pafupi ndilo laphokoso, si lakupfuulamokondwera kumapiri.
8. Katsalakampindi, ndipo ndidzakutsanuliraukali wanga ndi kukukwaniritsira mkwiyo wanga ndi kukuweruza monga mwa njira zako ndipo ndidzakubwezerazonyansa zako zonse.
9. Ndipo diso langa silidzalekerera, wosachita chifundo Ine, ndidzabwezera mwa njira zako ndi zonyasa zako zidzakhala pakati pako; ndipo mudzadziwa kuti Ine, ndine Yehova wakukantha.

Nkhani ili mundime iyi, ikukhudzanso mpingo wa masiku ano. Komabe anthu ena akhala akunena kuti Ezekieli anali kulembera Israeli wakale kotero kuti sizitikhudzamkomwe ayi. Koma tikunenetsa kuti Mulungu wa Chipangano Chatsopano ndi Mulungu wa Chipangano Chakale, kotero kuti adzapereka chilango ku mtundu uliwonse wa anthu m'masiku awo. Tsono tikunenetsa kuti mau awa, ayenera kukhala phunziro kwa mpingo wa Mulungu lero lino. Kutsimikiza kuti Mulungu adzalanga ndithu, kotero kuti ndicho chinthu chomwe adanena Paulo pa 2 Akorinto 5:11, pamene

adati, “Popeza tsono kuopsakwa Ambuye, tikopa anthu, koma tionetsedwa kwa Mulungu; ndipo ndiyembekezanso kuti tionetsedwam’zikumbu mtima zanu.”Kutsimikiza kuti ngakhale ziopsezo za zilango zikhoza kunyozekakwanthawi yaitari, koma sikuti zalephera ayi.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani pano ikunena kuti lero lino anthu akuseweretsa mpingo. Mpingo ukuoneka kuti ndichinthu chopepuka ndi chophweka, kotero kuti anthu ambiri amanena kuti ndi akristu chifukwa cha udindo, koma osadziperekakwa Ambuye Yesu Kristu. Iyi, ndiyo ngozi tikunena m’masiku athu ano. Kutsimikiza kuti bvuto lathum’mipingomo si kuchepakwa anthu mumpingo ayi, koma kusoweka kwa akristu oona.Kodi inu muli mgulu la akristu ati?

10. Taona tsikuli, taona lafika; tsoka lako laturuka, ndodo yaphukamphundu za maluwa, kudzitamakwaphuka.
11. Chiwawachaukachikhale ndodo ya choipa; sadzawatsalira ndi m’modzi yense, kapena waunyinjiwawo kapena wa chuma chawo; sipadzakhalanso kuwalira maliro.

12. Yafika nthawi, layandikiratsikulo, wogula asakondwere, ndi wogulitsaasamve chisoni; pakuti mkwiyo ukhaliraunyinji wawo wonse.

13. Pakuti wogulitsasadzabwera ku chogulitsacho, chinkanaakali ndi moyo, popeza masomphenyawo akunena unyinji wake wonse sadzapitapachabe, ndipo palibe m'modzi adzalimbitsa moyo wake m'mphulupulu yake.

14. Aombalipenga, nakonzeratu zonse, koma palibe womukakunkhondo; pakuti mkwiyo wanga ukhaliraunyinji wake wonse.

Ezekieli akufotokonza kuti zoipa za Yuda ndi Yerusalemu zinaoneka mwa anthu onse monga momwe nthambi imaphuka pamtengo m'nyengo yachilimwe.Momwemonso adani awo adzawakantha monga momwe akhala akuchitira ndeu ndi kuphana pakati pawo. Awa, ndiwo mau amene adanena Yesaya 5:7, pamene anati, "Chifukwa kuti munda wamphesa wa Yehova wa makamu ndiwo banja la Israeli, ndi anthu a Yuda, mtengo wake womkondweretsa; Iye anayembekeza chiweruziro, koma onani kuphana; nayembekeza chilungamo, koma onani kupfuula." Ndiye mwa mau awa,

tikunena kuti paliponse pamene pali chilango cha Mulungu, ndipotsimikizika kuti muzu wake ndi uchimo. Kutsimikiza kuti chilango chimadza pamene pali uchimo.Kunena kuti palibe munthu ndi m'modzi yemwe wochimwa, amene adzathawa chilango cha Mulungu ayi.Kutanthauza kuti munthu aliyense amene anachimwa, koma osalapa, adzafa ndithu.Palibe ndi m'modzi yense, amene azunza anthu osaukaadzatsala osaonongeka.Tikunena kuti ngakhale chiguluchikule motani ndipo ndimabvumechifuule kuti mpachikeni, mpachikeni, kuti adzapulumuka ayi.Ichi, ndichimene akutanthauza pamene akunena kuti, "Yafika nthawi, layandikiratsikulo, wogula asakondwere ndi wogulitsaasamve chisoni; pakuti mkwiyo ukhaliraunyinji wawo wonse."Anzanga, ndifuna kunenetsa kuti palibe gulu la anthu lomwe likhozakugonjetsachilango cha Mulungu chomwe chikubwera pa anthu onse wochimwa.Pano ndifuna mundimvetsetse kuti ngakhale anthu ochuluka motani atachitakugwirizana pa choipa, sikuti adzalekereredwaosalangidwa ayi.

Taonani mau onsewa akumangiriridwa pankhani yakuti "popeza masomphenyawo akunena unyinji wake wonse sadzapitapachabe,

ndipo palibe m’modzi adzalimbitsa moyo wake m’mphulupulu yake.”Kutsimikiza kuti chimene Mulungu wanena ndicho chidzachitika ndithu, ndipo kuti palibe munthu adzakhala ndi mphamvu mu uchimo wake ayi.Mau awa, akutanthauza kuti alipo anthu ena, amene amadzilimbitsa mu uchimo wawo, koma samangodzifooketsa chabe, koma kudziononga komwe. Iyi, ndiyo nkhani yomwe ili pa Masalmo 52:7, imene ikuti, “Tapenyani, suyumunthuyu amene sanamuyesa Mulungu mphamvu yake; amene anatamakuchuruka kwa chuma chake, nadzilimbitsam’kuipsa kwake.”

Ndiye verse 14, likuti, “Aombalipenga, nakonzeratu zonse, koma palibe womukakunkhondo; pakuti mkwiyo wanga ukhaliraunyinji wake wonse.”Kutanthauza kuti ngakhale asirikari atasonkhanitsidwandi kulimbikitsa anthu ochimwa onse, sizingathandizekupulumukakuchilango cha Mulungu.Kudzimikiza mau akuti, ngati Mulungu adana ndi ife chifukwa cha choipa, palibenso wina amene angatithandizekupulumukakuchilango chake.

Anzanga, pamau onsewa ndifuna muone kulephera kwa zinthu za dziko lapansi, kuti ngakhale m'nthawi yasautsosizingathe kupereka mpumulo ndi chitetezo. Ndiye tikunena kuti ndizoona kuti anthu atopa ndi nkhondo masiku ano, koma ngati mu mtima mwa munthu mukhalabe uchimo, Mulungu pa Yesaya 57:21, akunenetsa kuti, "Palibe mtendere,… kwa oipa."

19. Adzatayasiliva wawo kumakwalala, nadzayesa golidi wawo chinthu chodetsedwa; siliva wawo ndi golidi wawo sadzakhoza kuwalanditsa tsiku la mkwiyo wa Yehova, sadzakwaniritsa moyo wawo, kapena kudzaza matumba awo; pakuti izi ndi chokhumudwitsa cha mphulupulu zawo.

Pano ndifuna ndiyambe ndi mau akuti, masiku ano palichisimo chakuti ndalama ikhoza kuthana ndi bvuto lililonse m'moyo wa munthu. Pachifukwa chimenechi anthu akhala akupereka chuma chambiriku nkhondo za dziko ndi cholinga chakuti apeze mtendere.Tikunena kuti chuma chonse chomwe taperekachi, sitinachigwiritse ntchito bwino ayi.Kutanthauza kuti ndibwino kukhala ndi chuma, koma tiyenera kudziwa kuti sichingathetse mabvuto onse ayi.Ichi, ndichimene Mulungu akunena pano kuti

Israeli anakundika chuma chochuluka, koma sichinawathandizekuwatetezakuchilango cha Mulungu.

Nkhani iyi, ikuchoka pakuti Israeli anali kuganiza kuti chuma chawo ndichimene chikhozakuwatetezakwa adani awo komanso kuti chikhozakugula abwenzi, amene akhoza kuteteza moyo wawo. Komanso anali kuganiza kuti sangakhudzidwe ndi njala popeza anali ndi ndalama zochuluka.Tere taonani kuti anthuwa anaika mtima wawo pa chuma chawo, kotero kuti amakhulupirira kuti chikhozakuthetsa masautso awo onse.Koma taonani kuti mwachisangalo chachikulu, anaumitsa mitima yawo mu uchimo. Kutsimikiza kuti chuma chawo chinasandukachokhumudwitsa, kotero kuti chinakhalachowatchinga kuti atembunukirekwa Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, alipo anthu ambiri, amene chuma chawo chasandukamsamphawachionongeko. Kutsimikiza kuti pamene munthu apeza dziko lonse, ndiye kuti alipanjirayotaya moyo wake. Ili, ndilo funso lomwe anafunsa Ambuye Yesu pa Luka 9:25, pamene anati, “Pakuti munthu apindulanji, akadzilemezera dziko lonse lapansi nadzitayapo, kapena kulipapomoyo wake.”

Kutsimikiza kuti chuma sichithandiza m'nthawi yachilango cha Mulungu. Awa, ndi mau apa miyambo 11:4, amene akutsindika kuti, "Chuma sichithandiza tsiku la mkwiyo; koma chilungamo chipulumutsa ku imfa." Ndiye nkhani yonseyi ikuti, likudza tsiku la chilango cha Mulungu, pomwe chuma cha dziko lapansi sichidzakhoza kupulumutsa munthu kapena kumutumikira ayi.Tere, tikunenetsa kuti ndalama sizingathekuteteza munthu kuti asagwidwe ndi imfa ayi.

20. Ndipo chokometsera chake chokongola anachiyesachodzikuza nacho, napanga nacho mafanizo awo onyansa, ndi zonyasa zawo zina; chifukwa chake ndinapatsa ichi chikhalechowadetsa.
21. Ndipo ndidzachipereka m'dzanja la alendochikhalecholandika, ndi kwa oipa a m'dziko chikhalechofunkha; ndipo adzachiipsa.
22. Ndipo nkhope yanga idzawayang'anirakumbali, ndipo iwoadzadetsapobisika panga, nadzalowamoachifwamba, nadzamudetsa.

Pano pali chithunzi choopsa cha chiweruzo cha Mulungu chomwe chilimkudza.Taonani akunena kuti anapatsa Israeli Kachisi ngati chinthu chokongola kwambiri m'moyo mwawo, komanso anachitenga kuti ndicho chitetezo chawo.Ndipo Yeremiya 7:4, akunena kuti, "Musakhulupirire mau onama, kuti Kachisi wa Yehova, Kachisi wa Yehova, Kachisi wa Yehova ndi awa." Mwachisoni kuti anthuwa anaipsaKachisiyu pakuikamo mafano.Tere, pano Mulungu akubwezachipongwe chimenechi, pakuwachotserakachisiyo. Mwanjira ina akunena kuti anawachotsa ndi kuwapititsa kutari ndi Kachisi wa Mulungu, chinthu chimene chinali chowachititsa manyazi kwambiri. Ndiye phunziro likuti malamulo ndi zinthu zonse zothandizira mu mpingo, zimachotsedwakwa anthu onse onyoza Mulungu. Nkhani iyi, inaonetsedwa pamene Mulungu analoraakuba kuti alowe ndi kuchotsa malo opatulikitsa, malo amene amasonyeza kupezeka kwa Mulungu.

23. Sula unyolo, popeza dziko ladzala ndi mirandu yamwazi, ndi mudzi wadzala ndi chiwawa.

24. Chifukwa chake ndidzabwera nawo amitundu oipitsitsa, ndipo iwoadzalandira nyumba zawo ngati cholowa, ndidzaleketsanso kudzikuza kwa amphamvu, kuti adetsedwe malo awo opatulika.

Ndime zino, muli nkhani yakuti monga a Yuda anamanga dziko lawo ndi unyolowauchimo, momwemonso iwoadzadzimanga wokha ndi unyolo. Apa, akuonetsa kuti anthu amenewa anali kumangidwa unyolom'makosi awo pamene anali kutengedwa ukapolo. Tsono chithunzi ichi, ndichimene chikuonetsa kuti a Yuda wopanduka, adzamangidwanatengedwa kubwalo la milandu la Yehova kuti akaweruzidwe.Kutsindika kunena kuti, anthu amene amaphwanya malamulo a Yehova, adzapezekawomangidwa eni wokha.Kutanthauza kuti tchimo limamanga munthu wochita tchimolo.Kodi inu ndinu m'fulu?

Ezekieli 8

M'chapter chino, tipeza gawo lina lalikuru la ulosi wa Ezekieli. Mgawo limeneli ndimo tione za kuonongeka kotheratukwa Yerusalemu ndi Israeli. Apa, ndipo pamene ulemerero wa Mulungu unachokam'kachisi mu Yerusalemu.

1. Ndipo kunali chaka chachisanu ndi chimodzi, mweziwachisanu ndi chimodzi, tsiku lachisanu la mweziwo, pokhala ine m'nyumba mwanga, akulu a Yuda omwe analikukhala pamaso panga, dzanja la Yehova Mulungu linandigwerakomweko.

Tsono Ezekieli akanali ku Babulo, kotero kuti wakhala akupereka ulosi wowawa wokhudza Yerusalemu ndiye pano pali ulosi wa zomwe zinachitika ku Yerusalemu. Uwu, ndi ulosi wa m'chaka cha chisanu cha ukapolo wawo. Kutanthauza kuti Mulungu amasunga tsiku lina lililonse lomwe watumiza Uthenga Wabwino kwa ife ndi cholinga chakuti akatifunse pa ntchito yathuyi. Taonani Ezekieliakufotokonzansokuti, anali kukhala m'nyumba mwake mwina akulingalira za Uthenga wa Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo tikunena kuti, pamene tikhala ndi nthawi yopumakuzochitika m'dziko, timakhala ndi nthawi yolowam'chiyanjano ndi Mulungu. Komanso iwo amene akhala pansi nalingalira zomwe akhala akuphunzira, amaphunzitsidwa zambiri.

Tamvani kuti akulu a Yuda tsopano anali pamaso pa mneneri, Ezekieli.Kutanthauza kuti pamene akuluanatengedwa ukapolo, anayamba kumvera mau a mneneri Ezekieli, kusiyana ndi nthawi yomwe anali pamtendere ku Yerusalemu. Kutsimikiza kuti pamene Mulungu akwapula ana ake, nthawi yomweyo amatsegula makutu awo, kuti amve uphunguwa Yehova. Iyi, ndiyo nkhani ija adanena Yobu 36:8, 10, pamene anati, “Ndipo akamangidwa m’nsinga, nakakodwa ndi zingwe za mazunzo; Awatseguliranso m’khutu mwawo kuti awalangize, nawauzaabwererekuleka mphulupulu.”

Ndiye pamene tiwerenga verse 3 ndi 4, tikumva kuti mneneri Ezekieli anatengedwam’masomphenya kupita ku Yerusalemu. Iye, akunena kuti anatengedwa ndi chinthu chonga dzanja, chimene chikutchedwa Mzimu wa Mulungu. Mzimu uwu, umatchedwansochala cha Mulungu.Kutanthauza kuti ndi Mzimu wa Mulungu umene udamutengamuuzimu ndi kupitanaye ku Yerusalemu. Taonani anzanga, kuti Mulungu amatenga mtumiki wake wokhulupirika ndi chifuniro cha Mulungu kuti agwira ntchito yake, popeza Mzimuyoagonera mwa iye.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna titsirize ndi mau akuti masomphenya anaonetsedwakwa Ezekieli ndi cholinga chakuti tione kuti Mulungu ndiye wachifundo. Ndikunena mau amenewa chifukwa Mulungu samafuna kuchoka, kufikira atapulumutsa Israeli ngati akadatembenukirakwa Iye. Ndiye pamene tinena kuti Mulungu ndi chikondi komanso wachifundo, tiyenera kuzindikira kuti ndiye woyera komanso wolungama, amene sangalore tchimo lina lililonse m'dziko mwake.Tere, lero Mulungu sangapulumutse munthu chifukwa cha chiyero ndi chilungamo cha munthu ayi.Komanso palibe chimene Mulungu angalandire koposa chiyerochangwiro.Ichi, ndichimene chipezekamwakukhulupirira Ambuye wathu Yesu Kristu.Kodi inu mudamukhulupirira kale Ambuye Yesu?

Kwalerotilekeza pano. Ndipo timasanthula Ezekieli 7:1-8:4, momwe timakambirana za ulosi wa chionongeko chotsiriza cha mzinda wa Yerusalemu.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!